

2 Timoteo : 2:11-26

Mutu : Kupitiliza nkhani yochilimikapakutumikira

Ambuye

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Ambuye afuna kutitsogolera ndi mau apa Aroma 6:5, pamene Paulo akunena kuti, “Pakuti ngati ife tinakhalaolumikizidwa ndi Iye m’chifanizidwe cha imfa yake, koteronsotidzakhalam’chifanizidwe cha kuuka kwake.”

Tsono mupologalamu yatha tinali kukambirana kuchokera pa 2 Timoteo 2:1-13, momwe timasanthula zakuti wokhulupirira ayenera kuchilimikapakutumikira Ambuye. Ndipo lero pa 2 Timoteo 2:11-26, tipitiliza kuona za kuchilimikakwa wokhulupirira pakutumikira Ambuye.

11.Okhulupirikamauwa; pakuti ngati tidamwalira ndi Iye, tidzakhalanso moyo ndi Iye.

Mau awa, akutsimikiza kuti pamene wokhulupirira anatembenuka mtima, adzakhala ndi Kristu kwamuyaya.Ichi, ndichifukwa chake akunena kuti, ngati tidamwalira ndi Kristu ndiye kuti

tidzakhalanso ndi moyo ndi Iye. Iyi, ndi nkhanu yomwe Paulo adalemba pa Aroma 6:4, pamene anati, “Chifukwa chake tinaikidwam’manda pamodzi ndi Iye mwa ubatizo kulowa muimfa; kuti monga Kristu anaukitsidwakwa akufa mwa ulemerero wa Atate, chotero ifensotikayende m’moyo watsopano.” Kutsindika kunena kuti pamene tikudzakwa Ambuye, ndikumukhulupirira ngati Mpulumutsi, zikutanthauza kuti, imfa yake ikhala imfa yathu. Kotero kuti tiukitsidwanso pamodzi naye m’moyo watsopano. Kutsimikiza kuti Kristu amafunitsitsa kukhalanafe kudzera mwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

12. Ngati tipilira, tidzachitanso ufumu ndi Iye: ngati timkana Iye, Iyenso adzatikanaike.

Tsono nkhanu ili mundime ino, ikunena za kukhala pamodzi ndi Kristu m’moyo wake. Kunena kuti ngati tizunzika chifukwa cha dzina lake monga anachita Paulo, ndiye kuti tidzagawana zokoma za muulamuliro kapena zamuUfumu wake. Tamvani Aroma 8:17, akunena kuti, “Ngatitu ife, timva zowawa pamodzi naye, kuti tikalandirensa ulemerero pamodzi ndi Iye.” Koma ngati timkana pansi pano, ndiye kuti adzatikananso monga mwa mau apa Mateyu

10:33, amene akuti, “Koma yense amene adzandikana Ine pamaso pa anthu, Inensondidzamkana iye pamaso pa Atate wanga wa Kumwamba.” Tsono mau onsewa ndiwo akutsimikiza kuti Paulo anali kukhulupirira kuti chikhulupiriro chopanda ntchito ndi chakufa (Yakobo 2:17).

13.Ngati tikhala osakhulupirika, Iyeyu akhala wokhulupirika; pakuti sakhoza kudzikana yekha.

Wokondedwa anzanga apaulendo, tiyenera kutsindikamau akuti, Mulungu sangadzikaneyekha ayi.Kunena kuti sangathe kubvomereza woipa kuti ndiye wabwino ayi. Mwanjira ina tikunena kuti Mulungu alibe chinyengo monga Afarisi anali. Ichi, ndichifukwa chake Ambuye Yesu anawatcha kuti ndi wonyenga popeza anali kukhala ngati a Mulungu pamene sanali tero.Kutanthauza kuti inu ndi ine, tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro chosanyenga, monga Ambuye sangachite chinyengo china chilichonse.

14.Uwakumbutse izi, ndi kuwachitira umboni pamaso pa Ambuye, kuti asachite makani ndi mau osapindulitsa kanthu, koma ogwetsaiwoakuwamva.

Paulo wangofotokonza kumene pfundozikulu-zikulu zimene wokhulupirira ayenera kutsatira m'moyo wachikristu. Mukumbukira kuti Paulo wakhala akulimbikitsa Timoteo kuti ayenera kuyembekezera masautso m'moyo wake wachikristu, koma ayenera kupirira masautso onsewa chifukwa cha Kristu ndi Uthenga Wabwino. Ndiye akupitiliza kuti ziphunzitsa izi, Timoteo ayenera kuziphunzitsansokwa onse amene achita chisankho cha kuyenda ndi Kristu.

Ndiye panoakumulangizanso kuti sayenera kulowa pa mkangano wa mau achabe, osapindulitsa chifukwa cha nzeru zathu kapena kusiyana pa ziphunzitsa zathu. Kutanthauza kuti mipingoinakhazikitsidwa chifukwa cha kusiyana kwakatanthauzidweka mau ena m'Baibulo, koma sitienerakupikisana ayi. Ndikukhulupirira kuti Mulungu ndiye akaongolaife tonse patsiku ilo la chiweruzo. Koma chinthu chofunika kwambiri ndi kugwirizana pa zinthu zofunika monga za chipulumutso cha munthu woipa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, nkhani iyi ikutsindika pakuti lero mipingoikutaya nthawi pachabe kukangana ndi

kupikisanapazinthuzosathandizakweni-kweni. Tikunena kuti mipingoina, yatanganidwa kuyesa kukonza wokhulupirira anzawo, m'malo mokangalikakulimbikitsana ndi kukhala pachiyanjano cha pa Uthenga Wabwino.

Wantchito wosachita manyazi

15.Uchite changu kudzionetserakwa Mulungu wobvomerezeka, wa ntchito wopanda chifukwa cha kuchita manyazi, wolunjika nawo bwino mau a choonadi.

Paulo mundime ino akunena kuti cholinga cha utumiki sikukondweretsa anthu, koma kuchitachomwe ndi choyenera ndi kubvomerezekakwa Mulungu. Tsono kuti mtumiki akwanitse zimenezi, payenera kukhala kudzipereka pakusanthula ndi kusamalitsa mau a Mulungu. Paulo akutsindika pamenepa chifukwa akuona ngozi yomwe ilipo kuti mtumiki akachoka pamau a Mulungu, amafuna kutchuka kapena kumveka, osati kukwaniritsa cholinga cha Mulungu ayi.

Ndiye akutsindika kunena kuti mtumiki ayenera kulunjika nawo mau a choonadi. Kutsimikiza kuti mtumiki amene akhala m'mau a

Mulungu, ayenera kudziwa kuti mau a Mulungu ali ndi cholinga chimodzi chachikulu, chimene chimagawidwam'magawo ena olondolaang'ono-ang'ono. Kutanthauza kuti Baibulolinapangidwamotsatira ndondomeko yomwe iyenerakutsatidwa bwino pamene tiwerenga.Kunena kuti sikoyenerakumangotengaponunsu iyi ndi iyo, osatsatira momwe nkhani inayambira.Tikunenetsa kuti ndi chinthu chosabvuta kuchita zimenezi, koma ndikosayenera kuchita izi, pakusanthulaBaibulo.Kutsimikiza kuti Baibuloliyenerakuwerengedwamosamalitsa kwambiri.

Tsono pamene Paulo akunena kuti Timoteo akhale wantchito wopanda kuchita manyazi ndi kulunjika nawo bwino mau a Mulungu, chifukwa m'mau a Mulungu anadutsa mibadwo-mibadwo komanso anayenda m'njira zosiyanasiyana momwe Mulungu anapulumsira munthu.Koma tsinde lopulumutsira munthu ndilimodzi, popeza munthu amapulumsidwapakukhulupirira mu imfa yachipulumutso ya Ambuye Yesu Kristu.Koma taonani kuti munthu amaonetsa chikhulupiriro chake m'njira zosiyanasiyana. Ndikunena kuti m'nthawi ya Abele ndi Abraham, anali kutenga

mwana wa nkhusa ndi kumpereka nsembe kwa Mulungu. Koma lero, inu simungatenge mwana wa nkhusa ndi kukupereka nsembe ndi cholinga chakuti mukhululukidwe machimo anu ayi. Taonani kuti inu mukachita ichi, muchita chinthu chimene sichirim'ndondomeko yabwino masiku ano. Ichi, ndichifukwa chakuti Mwana wa nkhusa wa Mulungu, amene achotsa tchimo la dziko lapansi anabwera kale m'dziko lino. Mwana wa nkhusa uyu, ndi Yesu Kristu monga akunena pa Yohane 1:29, pamene Yohane m'batizi akuti, "Onani Mwanawankhusa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko lapansi."

Tsono mwachitsanzo chimenechi, ndifuna muone kuti Abele ndi Abraham, anali kuona m'tsogolo kuyembekezera kudza kwa Mwanawankhusa wa Mulungu, koma ife tikung'ana m'mbuyo kuona ntchito yomwe anachita Ambuye Yesu mwa imfa yake ya pamtanda ija.Ndiye pamene mtumiki atsindika pamau amenewa ndiye kuti akulunjika nawo mau a Mulungu.Mwachisoni lero atumiki ena amangoyambakulalikira mau a Mulungu osaona ndi kutsatira ndondomeko iyi.Aliponso anthu ambiri, amene amatsutsa mau a Mulungu, koma osadziwa mau a Mulunguwo.Tere,

tikunenetsa kuti munthu aliyense asanayambekulalikiramau a Mulungu, ayenera kukhala ndi nthawi yokwanira kuwerenga ndi kusanthula pa mutu umene afuna kuphunzitsa. Ichi, ndichimene Paulo akumuuzza mwana wake Timoteo kuti achilimikepakusanthula mau a Mulungu, kuti akhozekulunjika nawo bwino mau a choonadi. Kutsimikiza mau apa Mateyu 13:52, pamene Ambuye Yesu akunena kuti, “Chifukwa chake mlembi aliyense, wophunzitsidwa mu Ufumu wa Kumwamba, ali wofanana ndi munthu mwini banja, amene aturutsa chuma chake m’zinthu zakale ndi zatsopano.”

Wokondedwa anzanga apaulendo, mau onsewa akutsindika kuti, mtumiki wa mau a Mulungu ayenera kulunjika nawo Uthenga Wabwino, pakuona nyengo ndi kuona zosowa za anthu omvera Uthengawo kuti ulimbikitse miyoyo ya anthu kukhala ndi chiyembekezo cha kukakhala Kumwamba. Kodi inu mumapereka Uthenga wotere?

16. Koma pewa nkhani zopanda pake; pakuti adzapitirira kutsata chisapembedzo.

Paulo pano akubwerezansokuuza Timoteo mau amene ananenso pa 1 Timoteo 6:20, pamene anati, “Timoteo iwe, dikirachokusungitsa, ndi kulewazokamba zopanda pake ndi zotsutsana za ichi chitchedwachizindikiritsokonama.” Tsono Paulo akuchenjeza kolimba kuti nkhani zopanda pakezimakhala ndi cholinga chochotsa munthu kwa Mulungu wake. Mikanganoyotere ndiyo yotaitsa nthawi chabe komanso imachedwetsa ndi kulepheretsa ntchito yabwino.

Taonani munthu amene amakonda mikanganopazinthu za mau a Mulungu, ndiye amakonda kudzionetsa kuti ndi woyera pakuonekerakuthupi, koma simukamuonamunthuyu kukhala m'malo ya anthu okondakupemphera komanso simungayembekeze chithandizo chake pa ntchito yachipulumutso cha anthu ayi. Pachifukwa chimene Paulo akuchenjeza kuti pamene munthu ataya nthawi yake kukhala m'mikangano yachabe, anthu amakulandi kukhazikika m'moyo wachikunja.

17. Ndipo mau awo adzanyekachironda; a iwo ali Humenayo ndi Fileto.

Mundime ino, muli nkhani yakuti ziphunzitso zonyengazifanana ndi chironda chomwe chinyeka, popeza sichiononga malo okhawo, koma chimafalikirakumalo ena a thupi.Momwemonso chiphunzitso chonama sidzaononga gawo lokhalo la mau a Mulungu, lomwe likukambidwalo, koma chimakhudzanso ndi kuononga magawo ena a mau a Mulungu.Ndiye mwina inu mwafunsa kale kuti, kodi izi zimatheka bwanji?Yankho likuti ziphunzitso (doctrines) za mau a Mulungu, ndi zolumikizana kapena kuti ndizogwirizana kotero kuti pamene chiphunzitso chimodzi chionongeka, ziphunzitso zina zimakhudzidwa ndithu.

Ndiye Paulo akupereka chitsanzo cha Humenayo ndi Fileto kuti ndiwo anali kuphunzitsa ziphunzitso zonama.Humenayo ndiye uja Paulo pa 1 Timoteo 1:20, ananena za iye kuti, “Ndawapereka kwa Satana kuti aphunzirekusalankhula za mwano.” Koma pamene Paulo akumutchulanso zikuoneka kutianamubwezeretsanso atamudula mu mpingo, koma anayambiransokufesa mbeu ya bodza, yokhudza za kuukakwa akufa. Taonani aphunzitsi awa, anali kubvomereza za kuukakwa akufa, koma amanena kuti sikudzakhala kuuka kwa akufa kwa

thupi, komwe ndikutsutsa choona chomwe Ambuye wathu Yesu Kristu anaphunzitsa. Chiphunzitso ichi, ndichimene chinasokoneza wokhulupirira kotero kuti chiphunzitso ichi ndichimene chinapangitsa Paulo kulembamau pa 1 Akorinto 15:19, akuti, “Ngati tiyembekezera Kristu m’moyo uno wokha, tiri ife aumphawi oposa a anthu onse.” Ndiye tikunenetsa kuti chiphunzitso chilichonse chimene chimakana chiphunzitso cha moyo wa m’tsogolo, chimasokoneza chikhulupiriro cha akristu.

19.Koma ndithu maziko a Mulungu aimikapokhazikika ndi kukhala nacho chizindikiro ichi, Ambuye azindikiraiwo amene ali ake; ndipo adzipatule kwa chosalungama yense wakuchula dzina la Ambuye.

Mundime ino muli mau achitonthonzo amene akuti ngakhale pali ziphunzitso zonama ndi zosokoneza, zimene zimakhudza ndi kuononga mpingo, sizingathe kupanga malonjezo a Mulungu kukhala opanda pake ayi. Iyi, ndiyo nkhani akunena Paulo kuti, “Koma ndithu maziko a Mulungu aimikapokhazikika ndi kukhala nacho chizindikiro ichi.”Kutsindika kunena kuti nkondo yonse yomwe yakhalaikuthirika pa chiphunzitso cha Kristu,

siingakwanitsekugwedezachiphunzitsochi, popeza chinaima ndi kukhazikika pa maziko a Mulungu. Kunena kuti aneneri ndi Atumwi, a m'Chipangano Chakale ndi Chatsopano, ndiwo amene alichikhalireosagwedezeke, popeza ali ndi chizindikiro ndipo Ambuye awadziwa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna kunenetsa kuti, palibe ndi munthu m'modzi yense amene angakwanitse kuononga chikhulupiriro cha munthu amene Ambuye anamusankha. Ndiye tikunena kuti ngati dzina la Ambuye lili pa ife, tiyenera kuchoka pachodetsa chilichonse kuti tikhale ake a Kristu pokana kuti pa tsikuloasadzenene kuti sindinakudziwani inu nthawi zonse; chokani kwa Ine, inu akuchita kusayeruzika" (Mat. 7:23). Tsono pakupatukapachoipa, chidzathandiza anthu ena kuzindikira anthu amene ali a Mulungu. Wokhulupirira adzipatulekuchoipa chirichonse ndipo apatulikire Kristu. Mwachisoni kuti alipo anthu ena, amene amaphunzitsa choonadi, koma sakhala m'moyo wodzipatulakuuchimo ayi. Tere ndichifukwa chake timamva kuti abusaagwa pa tchimo ndi mkazi wina. Komabe tikunenetsa kuti Ambuye amadziwa ake, popeza amaona mtima wake wa munthu

pamene anthu amaona maonekedwe a moyo wakunja. Tsono taonani dziko lero, limapanga tchimo kukhala lokongola, kodi ife wokhulupirira timaoneka wokongola pakulengeza za Kristu?

Zipangizo zotengera

20.Koma m'nyumba yaikurusimulizotengera za golidi ndi silivazokha, komatunso za mtengo ndi dothi; ndipo zina zaulemu, koma zina zopanda ulemu.

21.Ngati tsono munthu adzayeretsa yekha pa izi, adzakhala chotengera cha kuulemuchopatulidwa, choyenera kuchita nacho Mbuye, chokonzero ntchito yonse yabwino.

Paulo pano akuonetsa wokhulupirira kuti ndiwo zipangizo.Ndiye akunena kuti, kuti chipangizochigwiritsidwe ntchito, chiyenera kukhala choyera. Taonani Paulo akunena kuti ngati inu ndi ine, tingasankhe ndi kukhumbakugwiritsa ntchito chikhochoyerapakumwa madzi, kuli bwanji ndi Mulungu amene anachita kuika nzeru yosankha chabwino ndi choipa mwa ife? Kutsindika kuti Iye, amagwiritsa ntchito chipangizochoyera chokha.Tere, lero lino Mulungu akufuna kugwiritsa ntchito zipangizo zoyera, osati zokongola ayi.Kunena kuti zipangizo zikhoza

kukhala zosaoneka bwino m'maso mwanu, koma ngati ziri zoyera Mulungu azigwiritsa ntchito zimenezo.

22.Koma thawazilakolako za unyamata, nutsate chilungamo, chikhulupiriro, chikondi, mtendere, pamodzi ndi iwoakuitana pa Ambuye ndi mitima yoyera.

Tsopano ndifuna muone kuti panonso Paulo waika pamodzi mau akuti, chikhulupiriro, chikondi ndi mtendere, zinthu zimene zimaonetsa moyo wachikristu.Kunena kuti inu ndi ine, sitienerakumangolankhula za chikhulupiriro, chikondi ndi mtendere, koma kuti zionekere m'moyo wathu.Tere, ndizimene Paulo afuna kuti Timoteo aonekere kapena kuti adziwike ndi moyo wachikhulupiriro, chikondi ndi mtendere.Kodi inu ngati mkristu, muli ndi moyo wotere?

23.Koma mafunsoopusa ndi opandamalangoupewe, podziwa kuti abalandeu.

Taonani Paulo akumuchenjeza Timoteo kusachitamakani kapena kulowa pamtsutsowa mau a Mulungu. Ndiye pofuna kupewa mitsutso imeneyi, Paulo akulangiza Timoteo kuti ayenera kupewa

mafunsoopusa ndi opandamalango.Tsono taonani kuti anthu amene amakonda mikangano, amadzitcha kuti ndi anzeru komanso ophunzira.Koma Paulo akunena kuti ndiwo wopusa ndi wosaphunzira. Iyi, ndi nkhani yomwe ili pa Miyambo 5:23, pamene pali mau akuti, “Adzafa posowa mwambo; adzasokerapopusa kwambiri.” Mwachisoni kuti pali anthu ena amene amafuna kumakanganapazinthuzosathandiza. Ndiye tikunenetsa kuti mtumiki wa Mulungu ayenera kupewa m’khalidwe umenewu chifukwa supindulitsa, koma kutaitsa nthawi chabe.

Kapolo wa Ambuye

24.Ndipo kapolo wa Ambuye sayenera kuchita ndeu, komatu akhale woyenera, waulere pa onse, wodziwa kuphunzitsa, woleza.

25.Ndipo akadzipulumutse ku msaphawa mdierekezi, m’mene anagwidwa naye, ku chifuniro chake.

Tsono tiyeni titsirize ndi mau akuti mtumiki wa Mulungu ndiwokhulupirira onse kuti afanana ndi kapolo ndipo ayenera kukhala wosakonda phokoso kapena mkangano ndi anthu ena ayi. Tsono mwina mukhoza kuona kuti mau awa, akutsutsana ndi mau

akuti wokhulupirira ayenera kumenya nkhondo, koma kapolo sayenera kumenya nkhondo kapena kukangana. Yankho likunena kuti pamene wokhulupirira akuimapachoonadi, iye ayenera kukhala wokhutitsidwa ndipo kuti anthu ayenera kudziwa kuti akuimapachoonadi osanjenjemera ayi.

Koma pamene mtumiki aphunzitsa za choonadi, ayenera kupereka Uthengawo moleza mtima, mosatsutsana naye munthu amene akupatsidwa Uthenga Wabwino. Kutanthauza kuti ngakhale iye atsutsanenawe, iwe uyenera kupitiliza kupereka Uthengawo moleza mtima.

Lero tilekeza pano. Ndipo tinali kusanthula 2 Timoteo 2:11-26, pamene timapitiliza kuona za kuchilimikakwa wokhulupirira pakutumikira Ambuye.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!